KODI FOTELEZA WOCHITA KUPANGIDWA KUCHOKELA KU MANKHWALA NDI CHANI?



duducoelho.com

Foteleza alipo wa mitundu yosiyanasiyana: Wachilengedwe komanso wochita kupanga. Foteleza wa chilengedwe amapangidwa kuchokela ku zinthu zimene zimachokela mu chilengedwe. Foteleza wochita kupanga kuchokela ku mankhwala amapangidwa ndi chiphatikizo chopangidwa ndi anthu cha mankhwala komanso zinthu zopanda moyo kapena kuti zomwe siziri zachilengedwe.

Foteleza wochita kupanga kuchokela ku mankhwala –

- amapangidwa mu nyumba za sayansi kapenanso nyumba zina zomwe si zapamunda ndipo amaphatikiza michere monga ya nitrogen, phosphorus, potassium, calcium, magnesium ndi yina mu milingo yosiyanasiyana;
- ***amagwira ntchito mwa change*** popeleka michere yofunikila ku nthaka, imene imatengedwa mwa change ndi mbeu;
- amapangidwa ndi kupakilidwa ku ma fakitale; ndiponso
- amasungidwa mu nyumba zosungilamo katundu ndi kugawidwa ku malo osiyanasiyana wotulutsira ndi kugulitsila katundu m'mdziko lonse.

Kugwiritsa ntchito foteleza wochita kupangidwa kuchokela ku mankhwalayu kumalimbikitsidwa kwambiri ndi maboma aku Africa pofuna kuchulukitsa zokolola. Maboma ambiri amapelekapo gawo la mtengo wa foteleze wopangidwa kuchokela ku mankhwalayu ndi cholinga chotsitsa mtengo – monga NPK – ngati gawo la ndondomeko ya zipangizo za ulimi zotsika mtengo.

african centre for biodiversity

www.acbio.org.za info@acbio.org.za Tel +27 (0)11 486 1156